

# ULAMULIRO WA GULU LA ANTHU VS. MULUNGU

**ndi Tony Alamo**

Moyo wanga ulemekeza YEHOVA MULUNGU ndikaona m'Malemba mmene MULUNGU amadalitsira aliyense wokhulupirira IYE ndi kutemberera onse akukayikira IYE (Deuteronomo 28:1-2, 15, Marko 16:16). Anthuwo, ambiri, akhala akulakwika nthawi zonse. Ichi ndi chifukwa chake demokalase (mfundo ya ulamuliro wa gulu la anthu) singakhoze konse kukhala yolondola!

Ofalitsa nkhani a lero apangitsa kuti zikhale zosavuta kuti Satana akuze mabodza ake, mwano wake, ndi malingaliro ake opotoka. <sup>1</sup> Pamene tiyandikira ku mapeto a nthawi, ndipamene akuonjeza kulakwitsa pa kampeni yake yonyenga dziko lonse (Chivumbulutso 12:9, 12-17).

Munthu angakhale ndi chikhulupiriro bwanji, kapena kukokera chikhulupiriro, ngati sakuwerenga MAWU a MULUNGU? Kukhulupirira MULUNGU kungakwaniritsidwe pakumva MAWU a MULUNGU (Aroma 10:17). Anthu akhonza kuwerenga MAWU a MULUNGU, koma AMAWAMVA IWO? "Iye amene ali ndi khutu [khutu lomva MZIMU WA MULUNGU], msiyeni iye AMVE chimene MZIMU [wa MULUNGU] anena kwa

mipingo [ndi ku dziko]" (Chivumbulutso 2:7). Vuto lalikulu ndilakuti anthu amafulumira kumva zonse zimene mzimu wa dziko unena kuchokera mkati mwa anthu, ndipo pang'onopang'ono kwam-biri kumva zimene KHRISTU anena pa MOYO, MZIMU, ndi UMOYO wa MULUNGU, umene ukhala mwa IYE komanso unaukitsa IYE kwa akufa. M'tsiku ndi m'nyengo zino, munthu akangokhulupirira MULUNGU, amazitenga kuti mbalume zoimila pamaso pa mulungu wa dziko lino kunena kuti, "PAKUTI ATERO YEHOVA"? Kodi ndi chikhulupiriro—chikhulupiriro chakuya—kapena mbalume? ICHI NDI CHIKHULUPILIRO!

YEHOVA amatiuza kuti tisamamvetsere Satana, monga Hava anachitira mmunda muja, ndiponso monga anthu akuchitira lero.<sup>2</sup> Ngati mumvetsera mdier-ekezi, mudzakhulupirira mdier-ekezi. "Inu mudzamusunga iye mu mtendere weniweni, amene malingaliro ake akhala pa INU [MULUNGU]: chifukwa akukhulupilirani INU" (Yesaya 26:3).

Machitidwe 1:1-11 amatiuza ife kuti tizimvera "zonse zimene YESU anayamba kuchita ndiponso kuphunzitsa, Mpaka tsi-



*Tony ndi Susan Alamo, okestra, ndi kwaya pa porogaramu yawo ya pa kanema m'zaka za m'ma 1970 ndi kumayambirilo a zaka zam'ma '80*

ku limene IYE anatengedwa kupita kumwamba, atatero IYE kudzera mwa MZIMU WOYERA anapereka malamulo kwa atumwi amene IYE anawasankha: Kwa amenenso IYE anadzionetsera YEKHA wamoyo atatha masautso AKE ndi zitsimikizo zosalakwika zambiri, naonekera kwa iwo masiku makumi anayi, ndi kunena zinthu za Ufumu wa MULUNGU: Ndipo, posonkhana nawo pamodzi, anawalamulira iwo kuti asachoke ku Yerusalemu, koma adikire lonjezano la ATATE, limene, IYE anati, munamva INE.

"Pakuti Yohane indetu anabatiza ndi madzi; koma inu mudzabatizidwa ndi MZIMU WOYERA asanathe masiku ambiri. Pamene iwowa atasonkhana pamodzi, anamufunsa IYE, nanena, AMBUYE, kodi INU pa nthawi ino mubwenzera ufumu kwa Israeli? Ndipo IYE anati kwa iwo, Sikuli kwa inu kudziwa nthawi kapena nyengo, zimene ATATE anaika m'ulamuliro WAKE. Koma inu mudzalandira mphamvu, MZIMU WOYERA atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni ZANGA m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya monse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero a dziko lapansi.

*(Zikupitilira pa tsamba 2)*

# ULAMULIRO WA GULU LA ANTHU vs. MULUNGU

(Zikupitilira kuchokera pa tsamba 1)

“Ndipo pamene IYE ananena zinthu izi, ali chipenyere iwo, IYE ananyamulidwa; ndipo mtambo unamulandira IYE kumchotsa pamaso pawo. Ndipo pamene iwo anali chipenyere kuyang’anitsitsa Kumwamba pomuka IYE, taonani, amuna awiri anaimilira pafupi pawo wobvala zoyera; Amenenso anati, Amuna inu a ku Galileya, muimiranji ndikuyang’ana Kumwamba? YESU yemweyu, amene walandidwa kwa inu kupita Kumwamba, adzabwera momwemo monga munamuona IYE ali kupita Kumwamba.”

Amuna amenewa ankakhala ndi YESU. Iwo anaona zonse zimene IYE anachita, anamva zonse zimene IYE analankhula, nawona IYE akuphedwa, monga IYE ananenera mmene zidzamu-chikire IYE.<sup>3</sup> Kenako, patatha masiku atatu ndi theka, IYE anauka kwa akufa, naper-eka malangizo, nakwera Kumwamba (Machitidwe 1:1-11). Izi zinawapatsa chikhulupiriro choposa chokwanira kukhala moyo wa Uthenga Wabwino, kenako kufa imfa ya mboni za Khristu chifukwa chomwecho. Uthenga Wabwino ndi wakale, watsopano, ndiponso wam’tsogolo.

Mboni ziwiri za MULUNGU ndi tso-golo laposachedwapa (Chivumbulutso 11:3-12). Iwo kuti aime pamaso pa mulungu wa dziko lino, amene ali mdier-kezezi ndi iwo onse amene ali katundu wa mdierkezezi (gululo), ayenera kukhala osachepera chikhulupiriro chochuluka monga Atumwi okhulupirika amene anali ophunzira a KHRISTU! Choy-amba, iwo samaonera TV, mafilimu, kapena kutsata ofalitsa nkhanu alionse— a zolemba, aulutsi, kapena zokhudza

3 Mat. 16:21, 17:22-23, 20:17-19, 28, 26:1-2, 24, Marko 8:31, 9:31, 10:32-34, Luka 17:25

kompyuta. Amawerenga ndi kukhulupirira MAU A MULUNGU, Chipangano Chakale ndi Chatsopano! IWO AMAK-HULUPIRIRA MULUNGU, nadana nazo zoipa zonse (Masalmo 97:10, Miyambo 8:13, Amosi 5:15)!

Choncho MULUNGU mwa YESU anati mu Chivumbulutso 11:3, “Ndipo ndidzapatsa mphamvu kwa mboni ZAN-GA ziwiri [amene ndi Enoch ndi mkazi wake, kapena Enoch ndi Daniel].”

Mu Danieli 12:8-10, Daniel anafunsa YEHOVA, “O AMBUYE wanga, ndi chi-yani chimene chidzakhale mapeto a zinthu izi? Ndipo IYE anati, Pita, Daniel: pakuti mawu atsekedwa ndi kumatidwa mpaka nthawi ya chimaliziro [imene ili TSO-PANO!]. Ambiri adzatsukidwa, nadzayeretsedwa, ndi kuyesedwa; koma oipa adzachita moipa: ndipo palibe mmodzi wa oipa adzazindikira; koma wanzeru [amene amaopa MULUNGU (Yobu 28:28)] adzazindikira.” “Koma iwe, muka mpaka chimaliziro: pakuti udzapumula, **NDI KUIIMA MU GAWO LAKO MASIKU OTSIRIZA**” (Daniel 12:13).

Daniel anali ndi chikhulupiriro chifukwa iye ankadziwa MAWU a MULUNGU, ndipo ankadziwa MULUNGU. MULUNGU anamupatsa tanthauzo la maloto a Mfumu Nebukadinezara, ndipo ngakhale mfumu inayiwala lotolo, Daniel anamuza mwatsatane chimene loto lake linali!<sup>4</sup>

Aulutsi a lero amatha, mu maminiti ochepa, kuwapanga anthu woyeretseta kuoneka

4 Dan. chap. 2

ngati anthu oipa kwambiri, ndipo ngakhale kupanga MAWU a MULUNGU, BAIBU-LO, kuoneka loipa. Akhonza kutipanga ife amene timakhulupirira Baibulo kuoneka ngati makoko a mtedza. Ndi MAWU a MULUNGU, mukhoza kumvetsa kuti iwo amene amaganiza choncho ndi anthu amene atsogozedwa ndi mzimu wa mdier-kezezi amene “ananyenga dziko lonse la-pansi” (Chivumbulutso 12:9).<sup>5</sup>

Aefeso 6:12 amadziwitsa kuti ife Akhristu tili pa nkhondo. Ndikunena za Akhristu enieni—Akhristu odzazidwa ndi MZIMU WOYERA. Tili pa nkhondo kaya tikufuna kapena ayi, kaya tikukondwera nazo kapena ayi. Nkhondo zonse lero ndi zauzimu. Muli pakati pa mbali ya nkhondo ya MZIMU wa AMBUYE, kapena mbali ya nkhondo ya mzimu wa mdierkezezi. Palibe amene alibe mbali.

Aefeso 6:12 akuti, “Pakuti ife [Akhristu] tilimbana osati ndi thupi ndi mwazi [wakuda, woyera, wofiira, wachikasu, waburawuni, etc.], koma ndi maukulu, ndi maulamuliro, ndi olamulira a mdima wa dzikoli, kulimbana ndi zoipa zauzimu

5 Mat. 24:5, 11-12, 24, 1 Tim. 4:1-2, 2 Tim. 3:13, Yuda 17-19, Chiv. 13:1-4, 11-15, 17:1-2, 8, 18:2-3, 23



## India

Wokonedwa wanga mwa Khristu, M'bale Tony Alamo,

Ndalandira phukusi lanu labwino la zolemba zanu. Zikomo kwambiri chifukwa cha chilimbikitso chanu mu ntchito ya Ambuye. Ndinagawa zolemba zanu zozizwitsa za Uthenga Wabwino. Anthu ambiri akuphunzira za Ambuye Yesu Khristu ndipo anthu ena akulandira ubatizo m'dzina la Ambuye Yesu Khristu. Chonde muwapempherere anthu amene angobatizidwa kumene. Komanso ndakutumizirani zithunzi za kugawa zolemba ndiponso zithunzi za ubatizo. Chonde pemphererani ntchito ya Uthenga Wabwino m'dera lathu ndi kupitiriza chilimbikitso chanu.

Kuno ife tonse tikukupemphererani, umoyo wanu wabwino, ogwira ntchito anu ku Alamo Ministries, mamembala anu a Alamo Christian Church mamembala anu ndiponso utumiki wanu wa zogawagawa. Chonde pitirizani kundipempherera, banja langa, malo osungirako ana amasiye, ndi ntchito ya Uthenga Wabwino ku dera lathu.

M'bale Wanu mwa Khristu,

M'busa A. David

Andhra Pradesh, South India



mmalo apamwamba.” Zotsala za chaputara sikisi zikutiuzwa mmene tingapil-irire zoipa zonse za masiku ano.

Mboni ziwiri mu chaputala leveni cha Chivumbulutso ndi zokonedwa kwam-biri za MULUNGU m’dziko lonse, kom-anso ndi anthu awiri odedwa kwambiri m’dzikoli. MULUNGU atapereka mpham-vu kwa iwo, IYE anati, “...mboni ZANGA ziwiri [MZIMU wa MULUNGU uli ndi mphamvu mwa iwo], ndipo zidzanen-era masiku chikwi chimodzi ndi mazana awiri mphambu makumi asanu ndi li-modzi, zitavala chiguduli [kutanthauza kuti adzakhala akusala<sup>6</sup>].

“Izo ndizo mitengo iwiri ya azitona, ndi zoikapo nyali ziwiri zakuima pamaso pa mulungu wa dziko lapansi [amene pan-opa ndi mdierekezi]. Ndipo ngati munthu wina akafuna kuipsa izo, moto utuluka m’kamwa mwao, nuononga adani awo [Adani? N’chifukwa chiyani anthu awiri oyoera kwambiri ali ndi adani? N’chifukwa chakuti pali mizimu iwiri, MZIMU WA AMBUYE, umene mboni ziwiri za MU-LUNGU izi zili nawo, ndi oipa, mzimu wosayera wa Satana, umene dziko lonse lili nawo.<sup>7</sup>]: ndipo munthu wina akafuna kuipsa izo, ayenera munjira imeneyi ku-phedwa.

“Izo [ziwiri] zili nawo ulamuliro wakut-seka kumwamba, kuti isagwe mvula ma-siku a uneneri wawo: ndipo ulamuliro zili

<sup>6</sup> Neh. 9:1, Est. 4:3, Masa. 35:13, Dan. 9:3 7 Mat. 6:22-24, 1 Akor. 2:11-16, Aef. chap. 2, 1 Yoh. 4:1-6

## Uganda

### AMBUYE ALEMEKEZEKE!

Ndi kumwetulira komanso kuthokoza kwakukulu ine ndi ana anga amene ali mu utumiki wanga tikufuna kutumiza zikomo wathu kwa inu chifukwa cha thandizo limene mwayamba kwa ife. Ndi m’dalitso wochokera kwa inu ndi kwa MULUNGU. Mwatipatsa chiyembekezo chopititsa pat-sogolo kufalitsa Uthenga Wabwino, maka-maka mwa ana anga. Ndikufuna kuti akule ndi kukhala m’chikhulupiriro chakuya.

Mundipempherere chifukwa mavuto alipo koma ndikuyenerabe kupita patso-golo. Ndimawerenga zolemba za uthenga wabwino zimene munatitumizira. Am-buye wabwino akudalitseni, M’busa Al-amo, ndi mpingo wa Tony Alamo Christian Ministries.

Kiyira Frank  
Entebbe, Uganda

nawo pamadzi kuwasandutsa mwazi, ndi kupanda dziko lapansi ndi miliri yonse, nthawi ili yonse zifunira. Ndipo pamene zitsiriza umboni wawo, chirombo [mzimu wa mdierekezi m’dziko la boma limodzi ndi mneneri wabodza wa Rome] chokwera kuturuka m’phompho chidzachita nazo nkondo, nichidzazilaka, nichidzazipha izo.

“Ndipo mitembo yawo idzagona m’misewu ya mzinda waukulu, umene mwauzimu utchedwa Sodomu ndi Ai-gupto, kumenenso AMBUYE wathu ana-pachikidwa. Ndipo anthu ndi mafuko ndi manenedwe ndi mitundu adzapenya mi-tembo yawo masiku atatu ndi theka lake [chachidziwikire kunali kulibe kanema zaka zikwi ziwiri zapitazo, koteru ulosiwu uwu ukunena za kanema], ndipo sadzalola kuti mitembo yawo iikidwe m’manda. Ndi-po iwo akukhala padziko lapansi [omwe MULUNGU analenga] adzakondwer-era pa iwo, nasangalala, nadzatumizirana m’phatso; popeza aneneri awiri awa [anthu a MULUNGU] anazunza iwo [ndi MAWU a MULUNGU] akukhala padziko lapansi.

“Ndipo patapita masiku atatu ndi theka lake MZIMU WAMOYO wochokera kwa MULUNGU unalowa mwa iwo, ndipo adayimirira chiliri; ndipo mantha akulu anawagwera iwo akuwaona. Ndipo anam-va mawu akulu akuchokera Kumwamba akunena nawo, kwerani kuno. Ndipo anakwera kunka Kumwamba mumtambo; ndipo adani awo anawaona.”

Izi zitatha, “Tsoka lachiwiri lacho-ka; ndipo, taonani, tsoka lachitatu lidza msanga. Ndipo m’ngelo wachisanu ndi chiwiri anawomba; ndipo panakhala mawu akulu m’Mwamba, ndikunena,

<sup>8</sup> Yes. chap. 53, Mat. 1:21, Yoh. 10:27-28, Mac. 5:30-31, 16:31, Aroma. 3:21-26, 10: 9, Aef. 2:13-16, Akol. 1:9-14, Aheb. 7:23-28, 9:11-15, 28, 1 Pet. 1:17-21, 2:21-24, 1 Yoh. 2:1-2, Chiv. 1:5

maufumu a dziko lapansi ayamba kukha-la a AMBUYE wathu, ndi a KHRISTU AKE; ndipo IYE adzachita ufumu kufikira nthawi za nthawi.”

“Ndipo mitundu inakwiya, ndipo un-adza mkwiyo WANU, ndi nthawi ya akufa, yakuti iwo aweruzidwe, ndi kuti INU mu-pereke m’photho kwa atumiki ANU aneneri, ndi woyera mtima, ndi iwo akuwopa dzina LANU, ang’ono ndi akulu; ndi kuwononga iwo akuwononga dziko lapansi” (Chivum-bulutso 11:3-12, 14-15, 18).

Taonani, AMBUYE wathu ndi MU-LUNGU wathu wakhazikitsa Ufumu wa Kumwamba pamaso panu, ndipo IYE wabwera ku dziko lapansi, MWANA WA NKHOSA WA MULUNGU, monga nsem-be ya machimo anu ndi anga.<sup>8</sup> Mipingo yosakhudzana ndi Malembo, ziwanda, ndi mbuli zimati “Palibe munthu wangwiro.” Iwo ali abodza. Panopa tili ANA a MU-LUNGU, Mafumu ndi Ansembe, Mtundu woyera! (Yohane 1:12, Aroma 8:14, 1 Petro 2:9, 1 Yohane 3:2, Chivumbulutso 5:9-10). Werengani Baibulo, King James Version yakale.

Mpingo woyamba unabadwira ku Is-rael (Machitidwe 1:1-5, 8, Chap. 2, 7:37-38). Panalibe amene anali Akatolika. Onse anali Aisraeli, ndipo onse Akhristu obad-wanso mwatsopano. Akatolika ndi achi-kunja (majentailo) ndipo ndiankhanza koopsa. Amadana ndi Ayuda nkumati sa-madana ndi Akhristu obadwanso mwat-sopano. Ozenga mlandu (Prosecutor) aliyense ndi oweruza (Judge) aliyense amene anandiimba mlandu ine wandip-atsa zilango zazitali, zankhanza ndipo

*(Zikupitilira pa tsamba 4)*

## Chile

*(Zomasulira kuchoka mu Spanish)*

Wokonedwa Mtumiki wa Mulungu Wam’mwambamwamba,

Madalitso ndi moni kwa inu ndi othandizana nanu akuyembekezera kudza kwa Yesu tsiku lililonse. Iye akupatseni mphamvu ndi kukulimbikit-sani kupita chitsogolo m’ntchito Yake tsiku lililonse limene lisali lophweka kapena lopepuka. Tikulitsutsa dziko lapansi kudzera mu ulaliki wathu. Angelo amange misasa mokuzungulirani, ndipo kumbukirani, sizili pach-abe. Muli kale ndi korona wanu wopambana pa kutembenuza miyoyo.

M’bale, ndinalandira phukusi lanu la zolemba ndi buku *la Mesiya*. Ndikupempha ngati mungathe kunditumizira m’phukuzi langa lotsatira Baibulo la chivindikiro cholimba. Zikomo ndi madalitso ochuluka.

M’bale Wanu,

Jose Omar Gonzalez Barria

Region de A Los Lagos, Chile

# ULAMULIRO WA GULU LA ANTHU VS. MULUNGU

(Zikupitilira kuchokera pa tsamba 3)

anakana kuti ine ndizitchula MAWU a MULUNGU. Komabe zilibe kanthu tso-pano. YESU AKUBWERANSO PADZIKO LAPANSI KACHIWIRI, NDI POSAKHALITSA! KONZEKANI. YAMBA NI NDI KUNENA PEMPHERO ILI:

AMBUYE wanga komanso MULUNGU wanga, ndichitireni chifundo ndine munthu wochimwa.<sup>9</sup> Ndikukhulupirira kuti YESU KHRISTU ndi MWANA wa MULUNGU wamoyo.<sup>10</sup> Ndimakhulupiriranso kuti IYE anafera pamtanda ndipo anakhetsa mwazi WAKE wantengo wapatali ndi cholinga choti machimo anga onse akhululukidwe.<sup>11</sup> Ndikukhulupiriranso kuti MULUNGU anakitsa YESU kwa akufa pogwiritsa ntchito mphamvu ya MZIMU WOYERA,<sup>12</sup> ndiponso kuti IYE anakhala kudzanja lamanja la MULUNGU ndipo panopa akumva pemphero langa lolapali.<sup>13</sup> Ndikutsegula zitseko za mtima wanga, ndipo ndikukuyitanani kuti mulowe mumtima mwanga, inu AMBUYE YESU.<sup>14</sup> Tsukani machimo anga ambirimbiri achoke onse mu mwazi wantengo wapatali umene INU munakhetsa m'malo mwanga pamtanda wa ku Kavari.<sup>15</sup> Ndikudziwa kuti mundimvera pemphero langali AMBUYE YESU; INU mukhululukira machimo anga ndi kupulumutsa moyo wanga. Ndikudziwa izi

chifukwa MAWU ANU, Baibulo, limanena zimenezi.<sup>16</sup> MAWU ANU amati INUYO simudzakana kumvetsera pemphero la munthu aliyense, ndipo ine ndili m'gulu la anthu amenewo.<sup>17</sup> Choncho, ndikudziwa kuti INUYO mukundimvetsera pamene ndikupemphera ndipo ndikudziwanso kuti INUYO muniyankha komanso mundipulumutsa.<sup>18</sup> Ndipo ndikukuthokozani AMBUYE YESU, chifukwa chopulumutsa moyo wanga, ndipo ndisonyeza kuyamikira mwa kuchita zinthu zimene INUYO munalamula komanso kupewa kuchita uchimo.<sup>19</sup>

Pambuyo pa chipulumutso, YESU ananena kuti munthu ayenera kubatizidwa pomizidwa thupi lonse m'madzi, m'dzina la ATATE, ndi la MWANA, ndi la MZIMU WOYERA.<sup>20</sup> Muziphunzira mwakhama Baibulo la *Buku Lopatulika Ndilo Mau a Mulungu*, [King James Version] ndipo muzichita zimene Baibulolo limanena.<sup>21</sup>

KHRISTU ndi MULUNGU ATATE tso-pano akhala mwa inu kudzera mwa MZIMU WOYERA. Pali njira imene mungalandilire gawo lokulirapo la umulungu wa MULUNGU mwa inu. Pamene umulungu wa MULUNGU wakukhala mwa inu uchuluka, m'pamene muchulutsa kukwanitsa kulimbana ndi mayesero amene mosavuta anasuntha Akhristu ambiri kukhala chitali ndi chipulumutso. Pemphererani ubatizo mwa MZIMU WOYERA. Pa malangizo a mmene mungalandilire ubatizo mwa MZIMU WOYERA ndi kulandira chambiri cha chikhalidwe choyera cha MULUNGU, funsani zowerenga zathu kapena

imbani lanya. Pakuti popanda chiyezo, palibe munthu adzaona MULUNGU (Ahebri 12:14).

AMBUYE akufuna kuti inuyo muziwuza ena za chipulumutso chanu. Mungathe kukhala wofalitsa uthenga wabwino wa M'busa Tony Alamo. Tizikutumizirani mabuku mwa ulere. Imbani foni kapena tumizani imelo kwa ife kuti mudziwe zambiri. Tikukupemphani kuti muwuzeko ena uthengawu.

Ngati mukufuna kuti dziko lipulumutside monga m'mene YESU akulamulira, mukufunika kupereka chakhumi kwa MULUNGU. MULUNGU anati, "Kodi munthu angabere MULUNGU? Inde, mwandibera kale. Koma akuti, Ife tikumubera bwanji MULUNGU? Mu chakhumi ndi mu zoper-eka. Anthuwo ndi otembereredwa chifukwa akundibera, ngakhale mtundu wonsewu [dziko lonse lapansi]. Bweretsani nonse chakhumi ['chakhumi' ndi gawo limodzi la magawo khumi (10%) ya malipiro anu] m'nkho kwanga zanga n'cholinga choti pakhale nyama [chakudya cha Uzimu] mu nyumba YANGA [anthu opulumutsidwa] kuti muniyese, akutero AMBUYE wa MAKAMU, kuti muone ngati sindidzakutsegulirani mazenera a Kumwamba ndi kukukhuthulirani madalitso amene mudzasowa malo owalandirira." Ndipo ndidzadzudzula anthu okudyerani masuku pamutu ndipo sadzawononga zipatso za nthaka yanu; ngakhale lenso mphesa wanu sudzalephera kubala zipatso pa nyengo yake m'minda yanu, wato AMBUYE wa MAKAMU. Ndipo mitundu yonse idzakutchani odala: chifukwa dziko lanu lidzakhala labwino, wato AMBUYE wa MAKAMU" (Malaki 3:8-12).

9 Sal. 51:5, Aro. 3:10-12, 23 10 Mat. 26:63-64, 27:54, Luka 1:30-33, Yoh. 9:35-37, Aro. 1:3-4 11 Mac. 4:12, 20:28, Aro. 3:25, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 5:9 12 Sal. 16:9-10, Mat. 28:5-7, Marko 16:9, 12, 14, Yoh. 2:19, 21, 10:17-18, 11:25, Mac. 2:24, 3:15, Aro. 8:11, 1 Akor. 15:3-7 13 Luka 22:69, Mac. 2:25-36, Aheb. 10:12-13 14 1 Akor. 3:16, Chiv. 3:20 15 Aef. 2:13-22, Aheb. 9:22, 13:12, 20-21, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 1:5, 7:14 16 Mat. 26:28, Mac. 2:21, 4:12, Aef. 1:7, Akol. 1:14 17 Mat. 21:22, Yoh. 6:35, 37-40, Aro. 10:13 18 Aheb. 11:6 19 Yoh. 5:14, 8:11, Aro. 6:4, 1 Akor. 15:10, Chiv. 7:14, 22:14 20 Mat. 28:18-20, Yoh. 3:5, Mac. 2:38, 19:3-5 21 Deut. 4:29, 13:4, 26:16, Yos. 1:8, 22:5, 2 Tim. 2:15, 3:14-17, Yak. 1:22-25, Chiv. 3:18

Ngati mukufuna kudziwa zambiri kapena ngati mukufuna mabuku kapenanso nkhani zina zimene zimakusangalatsani, tiimbireni foni kapena tilembereni.

**Tony Alamo, World Pastor, Tony Alamo Christian Ministries Worldwide • P.O. Box 2948, Hollywood, CA 90078**

**Lanya ya pemphero ndi uthenga maola 24: +1 (661) 252-5686 • Fax +1 (661) 252-4362**

**www.alamoministries.com • taoffice@alamoministries.com**

Tony Alamo Christian Ministries Worldwide imalandira anthu onse ndipo imapereka zinthu zofunika kwa onse amene ali ku U.S. amene akufunitsadi kuti ayambe kutumikira AMBUYE ndi mtima wawo wonse moyo wawo wonse ndi m'phamvu zawo zonse

**Mapemphero amachitika usiku uli wonse nthawi ya 8 Koloko usiku ndi Lamulungu nthawi ya 3 Koloko madzulo ndiponso 8 Koloko usiku ku Tchalitchi cha kudera la Los Angeles: 13136 Sierra Hwy., Santa Clarita, CA 91390, +1 (661) 251-9424**

**Magalimoto a ulere opita ndi kuchokera ku mapemphero amaperekedwa pa kona ya Hollywood Blvd. ndi Highland Ave., Hollywood, CA tsiku lili lonse nthawi ya 6:30 madzulo, Lamulungu lili lonse nthawi ya 1:30 madzulo ndi 6:30 usiku.**

**Mapemphero amachitika mu Mzinda wa New York Lachiwiri lili lonse nthawi ya 8 Koloko usiku ndi madera ena usiku okhaokha. Chonde imbani foni kuti mumve zambiri: +1 (908) 937-5723. ZAKUDYA ZIMAGAWIDWA PA MAPETO PA MAPEMPHERO ALI WONSE**

**Funsani buku la M'busa Alamo, lakuti Mesiya, losonyeza KHRISTU kuyambira ku Chipangano Chakale mu maulosi oposa 333.**

**Khalani wogwira ntchito yokolola miyoyo ya anthu pakukhala ogawira mabuku a M'busa Alamo**

**Mabuku ndi zinthu zonse zomvetsera n'zaulere, ndipo simulipira ndalama yotumizira**

**Ngati wina akukuuzani kuti mupereke ndalama pa zinthu zimenezi, chonde imbani pa +1(661) 252-5686.**

**M'BUKU ILI MULI CHIKONZERO CHENICHENI CHA CHIPULUMUTSO (Machitidwe 4:12).**

**MUSALITAYE, PATSANI ENA KUTI AWERENGE.**

**Anthu amene muli m'mayiko ena, tikukulimbikitsani kuti mumasulire n'chinenero chanu mabukuwa. Ngati mukusindikizanso bukuli, musaiwale kuika mawu ali m'munsiwa omwe ndi okhudzana ndi zamalamulo:**

© Copyright December 2014, 2016 All rights reserved World Pastor Tony Alamo © Registered December 2014, 2016  
CHICHEWA/NYANJA—VOLUME 20600—MOB RULE VS GOD